


# ANDREA KAGGWA WOYERA PARISH

CONSTITUTION

KAGGWA | V1 | 4 August 2024

# MAWU OTSOGOLERA

# ZAMKATIMU

MAWU OTSOGOLERA 1

ZAMKATIMU 2

1. MPINGO WA PAMALO PONSE: MU ARKIDAYOSIZI, M'PARISH NDI M'PHAKATI 0

2 UTSOGOLERI WA PARISH 2

2.1 BAMBO MFUMU 3
2.1.1 UDINDO WA BAMBO MFUMU 3
2.2 PARISH EXECUTIVE 3
2.2.1 NTCHITO ZA PARISH EXECUTIVE 3
2.2.2 NTCHITO ZA WACHIWIRI KWA WA PAMPANDO WA PARISH 3
2.2.3 NTCHITO ZA WOTSATIRA KWA WACHIWIRI KWA WAPAMPANDO 4
2.2.4 NTCHITO ZA MLEMBI 4
2.2.5 NTCHITO ZA WACHIWIRI KWA MLEMBI 4
2.2.6 NTCHITO ZA MSUNGICHUMA 4
2.3 PARISH TEAM 5
2.4 BUNGWE LOYANG'ANIRA CHUMA (FINANCE COMMITTEE) 5
2.4.1 NCHITO ZA BUNGWE LOYANG'ANIRA CHUMA 6
2.4.2 NTHUMWI ZAKE 6
2.5 PARISH COUNCIL 7

3. UTSOGOLERI WA PA CHURCH 7

3.1 CHURCH EXECUTIVE 7
3.1.1 NTCHITO ZA WAPAMPANDO 8
3.1.2 NTCHITO ZA WACHIWIRI KWA WAPAMPANDO 8
3.1.3 NTCHITO ZA MLEMBI 8
3.1.4 NTCHITO ZA WACHIWIRI KWA MLEMBI 9
3.1.5 NTCHITO ZA MSUNGICHUMA 9
3.1.4 NTCHITO ZA M'GULUPA 9
3.2 CHURCH COUNCIL 9
3.2.1 ZOLINGA ZA CHURCH COUNCIL 9
3.2.2 UDINDO WA CHURCH COUNCIL 10
3.2.3 NTHUMWI ZA CHURCH COUNCIL 10
3.2.4 ZOFUNIKIRA KUTI WINA AKHALE NTHUMWI YA CHURCH /PARISH COUNCIL 11
3.2.5 KUCHOTSEDWA PA UDINDO 11

4 KUMANGA MPINGO OZIDALIRA 11

4.1 KUPEZA CHUMA CHOYENDETSA CHURCH 12
4.2 KUGWIRA NTCHITO ZA CHITUKUKO LIMODZI PAKATI PA CHURCH COUNCIL NDI PARISH COUNCIL PA KAGGWA PARISH 13
4.3 KUYENDETSA NTCHITO ZACHIFUNDO 14

## 1. MPINGO WA PAMALO PONSE: MU ARKIDAYOSIZI, M'PARISH NDI M'PHAKATI

i. Mulungu amafuna kuyeretsa ndi kupulumutsa anthu kuti akhale Mbumba imodzi. Mbumba imeneyi iyenera kukhala yomvera, yoyera mtima ndi kutumikira Iye. Amene amakhulupira Yesu Khristu pakulandira ubatizo ndi mzimu woyera, amasanduka Mbumba ya Mulungu (1 Petro 2:9-10).

ii. Cholinga cha Mbumba imeneyi nkulimbikitsa za Ufumu wa Mulungu pakufalitsa mawu ake. Mbumbayi ikhale banja lamoyo, lokondana ndi lotsata zoona. Ndipo ikhale muuni wounikira ndi mchere wa pansi pano (Mateo 5 : 13-16).

iii. Dzina la Mbumbayi ndi Mpingo wa Yesu Khristu (Mateo 16:18) chifukwa adaugula ndi magazi ake (Ntchito 20:28), naudzaza ndi Mzimu wake ndi kuupatsa zonse zofunikira popeza kuti uyenera kukhala Mpingo wooneka poyera.

iv. Arkidayosizi ndi chigawo cha Mbumba Ya Mulungu chimene chidaikidwa m'manja mwa Arkiepiskopi kuti achisamalire mothandizidwa ndi ansembe.

v. Kuti Arkiepiskopi athe kusamalira bwino Mbumba yamulungu, amagawirako udindo wake woyendetsa mpingo kudzera ku Parish, out station ndi m'phakati.

vi. Choncho, mkhristu aliyense amagwirizana ndi Ambuye Yesu pa udindo wake wa unsembe, uphunzitsi, utumiki. Palibe Mkhristu amene anganene kuti ntchito zimemezi si zake.

vii. Bambo Mfumu pamodzi ndi Ansembe anzawo ndi a khristu eni ake ayenera kutumikira pamodzi mwaubale ndikuthandizana monga momwe mchere umakometsera chakudya. Akhrsitu ayenera kuvomera udindo wawo pa ntchito yotumikira mpingo.

## 2 UTSOGOLERI WA PARISH

**BAMBO MFUMU**

**Parish Chairman**

**PARISH EXECUTIVE**

**Nthumwi**
Bambo Mfumu (**Chairman**)
Vice Chairperson
Secretary
Vice Secretary
Treasurer (Treasurer wa finance Committee)

**PARISH TEAM**

**Nthumwi**
Bambo Mfumu (**Chairman**)
Ansembe
Asisiteri
Abulazala
Agulupa

**BUNGWE LA ZA CHUMA (FINANCE COMMITTEE)**

**Nthumwi**
Bambo Mfumu (**Chairman**)
Ansembe Othandiza bambo Mfumu
Akhristu eni ake osachepera asanu ndi awiri (7) koma asapitilire asanu ndi anayi (9)

**PARISH COUNCIL**

**Nthumwi**
Bambo Mfumu (**Chairman**)
Parish Team
Parish executive
Ma Chair a miphakati

**CHURCH EXECUTIVE**

**Nthumwi**
**Chairperson,** Vice Chairperson, Secretary, Vice Secretary, Treasurer, Agulupa

**CHURCH COUNCILS**

**Nthumwi**
Church executive chairman (**Chairman**), Church executive, Chairman wa mphakati, Chairman wa bungwe la pa Church

## 2.1 BAMBO MFUMU

Bambo Mfumu ndi mutu wa Parish. Udindo wake wotsogolera chigawo chimenechi cha Arkidayosizi amaulandira kuchokera m'manja mwa Arkiepiskopi. Pansi pawo amathandizidwa ndi magulu angapo a mu mpingo kuti mpingowo uyende bwino.

### 2.1.1 Udindo wa Bambo Mfumu

Udindo wa Bambo Mfumu ukupezeka mu buku la Parish Council Constitution ya Lilongwe Arkidayosizi (Mutu 4.10). Mwazina, Bambo Mfumu amakhala chairman wa Parish council ndi Parish executive. Ngati iye palibe, Parish council singakumane pokhapokha iye atasankha omuimilira.

## 2.2 PARISH EXECUTIVE

Parish executive idzasankhidwa ku Parish Council ndipo idzatsogoleredwa ndi Bambo Mfumu. Ntchito za parish executive ndi a dindo a mu parish executive zafotokozeledwa pansipa.

### 2.2.1 Ntchito za Parish executive

i. Kulandira ndi kukonza mitu yokambidwa ku Parish Council pamodzi ndi Bambo Mfumu.
ii. Kuwonetsetsa kuti mfundo zomangidwa mu Parish Council zikutsatidwa.
iii. Kuwonetsetsa ndi kuthandiza kuti moyo wa tsiku ndi tsiku wa Parish ukuyenda bwino.
iv. Kuimirira Parish ku misonkhano ya Akhristu eniake.

### 2.2.2 Ntchito za wachiwiri kwa wa Pampando wa Parish

i. Kukonza mfundo za msonkhano mothandizana ndi Bambo Mfumu ndi komiti yapamwamba.
ii. Kuchititsa misonkhano yonse ya Parish Council.
iii. Kumvetsera maganizo a nthumwi mu msonkhano kuti potero athe kumanga chimodzi.
iv. Kuwona kuti mfundo zomangidwa ndi zotsimikizika zilikutsatidwa
v. Kuyang'anira ntchito za Mlembi, Msungichuma ndi amaudindo ena onse a pa Parish

### 2.2.3 Ntchito za Wotsatira kwa Wachiwiri kwa wapampando

i. Wotsatira kwa Wachiwiri kwa Wapampando adzachita ntchito zonse za Wapampando ngati iye palibe komanso ngati wapemphedwa kutero.

### 2.2.4 Ntchito za Mlembi

i. Kulandira zokambirana za misonkhano ya Church Council ndi ku miphakati.
ii. Kulandira mitu ya nkhani zoyenera kulowa pa mfundo zokambirana ku Parish Council.
iii. Kulengeza misonkhano ndi kutumiza mfundo ndi ndondomeko zoyenera kukambirana (agenda).
iv. Kulumikizana ndi a pa mpando a Church pa zochitika za pa Church
v. Kulemba mwatsatanetsatane mndandanda wa zokambidwa mu msonkhano ndi kutumiza kwa nthumwi pasanapite sabata ziwiri koma zitawonedwa ndi Bambo Mfumu ndi wachiwiri kwa wapampando.
vi. Kuwerenga zokambirana za msonkhano wam'mbuyo ndi kukonza ngati nkofunika.
vii. Kusunga maina a nthumwi m'mene ziliri panthawiyo.
viii. Kusunga bwino mabuku a zokambidwa za msonkhano wa Parish Council ndi kukhala okonzeka kuonetsa Ansembe kapena AmbuyeArkıepiskopi.

### 2.2.5 Ntchito za wachiwiri kwa Mlembi

Wachiwiri kwa Mlembi adzathandizira mlembi pogwira ntchito za ulembi.

### 2.2.6 Ntchito za Msungichuma

i. Kulandira malipoti a ndalama ndi zopercka za Church Council ndi ku miphakati.
ii. Kulemba bwino ndi mosamala ndalama zolowa ndi zotuluka m'thumba la Parish ndiponso zomwe zidagwira ntchito. Ayenera

kukhala wokonzeka kuonetsa mabuku ake ku Finance Committee ya Parish Council.

iii. Kulipira zinthu zokhazo zimene zavomerezedwa ndi Parish Council m'ndondomeko ya za chuma cha Parish (budget) zomwe Bambo Mfumu wavomereza.

iv. Kupereka lipoti la ndalama pa msonkhano uliwonse wa Parish Council.

v. Kupereka lipoti la ndalama la chaka chonse kwa Msungichuma wa Arkidayosizi.

vi. Kupeza njira zothandiza kuti Parish ikhale yodzidalira mogwirizana ndi Bambo Mfumu.

## 2.3 PARISH TEAM

Parish Team ndi bungwe lomwe limapangidwa ndi Bambo Mfumu ndi Ansembe anzawo, Asisiteri, Abulazala ndi Agulupa omwe amagwira ntchito pa Parish limodzi.

A parish team amakonza ndi kukhazikitsa Mfundo zokhuza chipembezo ndi moyo wauzimu pa parish.

## 2.4 BUNGWE LOYANG'ANIRA CHUMA (FINANCE COMMITTEE)

Parish ili yonse iyenera kukhala ndi Bungwe loyang'anira chuma potsata Malamulo a Mpingo wonse pa dziko la pansi (Canon Law) ndiponso motsogozedwa ndi ndondomeko imene Episkopi wadayosiziyo adakhazikitsa. Anthu okhala m'Bungweli amasankhulidwa potsata lamulo Ia Mpingo (Canon 537).

Cholinga chawo chachikulu nkuthandiza Bambo Mfumu kusamala katundu wa Parish potsata Canon 532 lomwe limati: "Bambo Mfumu amaimira Parish pa zinthu zonse zokhudza malamulo." Bambo Mfumu aonetsetse kuti katundu wa Parish akusamalidwa potsata mfundo za Canon 1281 mpaka 1288. Komiti iyi imayendesa chuma cha parish ndikupanga kalondolondo wa kagwiritswidwe ntchito ka chumacho.

### 2.4.1 Nchito za Bungwe loyang'anira chuma

i. Kulangiza Bambo Mfumu pa ntchito za chuma cha Parish motsata Canon 537.
ii. Kulondoloza ntchito za chuma.
iii. Kulimbikitsa ndi kuyang'anira ntchito za chuma m'miphakati, m'ma outstation ndi m'mabungwe ena onse pa Parish.
iv. Kuonetsetsa kuti Parish ndi yoyima pa yokha.
v. Kupereka maganizo ku Parish Council pa mlingo wa mtulo ndi masika mogwirizana ndi ma Deanery.
vi. Kuchita kalondolondo wa ndalama zopita kwa Msungichuma wa Dayosizi ndiponso ndalama zoikidwa ndi zotengedwa ku Bank.
vii. Kupereka ndondomeko ya za chuma ku Parish Council kamodzi pa miyezi inayi ili yonse.
viii. Kusunga ndi kulondoloza kalembera wa chuma chonse cha Parish.
ix. Kukonza ndondomeko ya momwe ndalama zigwiritsidwire ntchito pa Parish (Budget) Chaka chili chonse ndi kupereka ndondomekoyi ku Parish Council ndiponso kwa Msungichuma wa Dayosizi.
x. Kuonetsetsa kuti ndalama zonse zoperekedwa monga za mmbale, masika, mtulo za ku miphakati ndi ma outstation zikufika ku Parish. (Ndalama ili yonse yolandiridwa ilembedwe mu buku la malisiti {Receipt Book}).

### 2.4.2 Nthumwi zake

i. Bambo Mfumu ndiye wamkulu woyang'anira katundu wa Parish. Ndiyenso wamkulu woyang'anira Bungwe loyang'anira Chuma la Parish.
ii. Ansembe othandiza Bambo Mfumu (curates) ayenera kukhala nthumwi za Bungwe loyang'anira Chuma la Parish.
iii. Nthumwi Zina za Bungwe loyang'anira Chuma zidzasankhidwa m'njira izi :

a. Bambo Mfumu adzafunsa madera, ma outstation ndi miphakati maina a anthu amene akuwayesa oyenera kukhala nawo m'Bungwe loyang'anira Chuma.
b. Bambo Mfumu adzasankhapo nthumwi pa mainawo atafufuza bwinobwino poyang'anira makhalidwe awa: kukhulupirika, kudzipereka, mphatso kapena luso monga kuwerengera chuma, mbiri yakayendetsedwe ka chuma, ndi kukhala wa chikhulupiriro.

iv. Nthumwizo zidzapikisana pa chisankho cha Bungwe loyang'anira Chuma la Parish ndipo Bambo Mfumu ndiye woyendetsa chisankho.

v. M'bungwe loyang'anira Chuma la Parish mukhale Akhristu eni ake osachepera asanu ndi awiri koma asapitilire asanu ndi anayi.

### 2.5 PARISH COUNCIL

Parish Council ndi bungwe la nthumwi zoimira Mbumba yonse ya Mulungu yokhala m'Parishmo. Cholinga chake ndi kupititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu pansi pano.

Udindo wa Parish Council, nkukumana ndi kukambirana momwe ntchito zosiyanasiyana za Parish zikuyendera potsata ndondomeko ya Arkidayosizi (LAMULO 536#2).

Nthumwi za Parish Council ndi Bambo Mfumu (Chairman), Parish Team, Parish executive, a pampando a Church, a pampando a mphakati ndi a Treasurer a Church.

Ntchito ndi malamulo oyendetsera Parish council zikupezeka pa mutu 4 wa buku loyendetsera ma Parish muno mu Lilongwe Archdiocese.

## 3. UTSOGOLERI WA PA CHURCH

### 3.1 CHURCH EXECUTIVE

Oyenera kukhala mu maundindo a church executive ndi awa;

i. Wapampando ndi Wachiwiri wake.
ii. Mlembi ndi Wachiwiri wake.
iii. Msungichuma
iv. Agulupa (Ex officio)

### 3.1.1 Ntchito za Wapampando

i. Kukonza mfundo za msonkhano (agenda) mothandizana ndi Church executive.
ii. Kuyendetsa misonkhano yonse.
iii. Kumvetsera maganizo a nthumwi mu msonkhano kuti potero zithe kumanga chimodzi.
iv. Kuwona kuti mfundo zomangidwa zikutsatidwa.
v. Kuwonetsetsa kuti maudindo onse mu church council akugwira ntchito yawo bwino
vi. Kulondoloza zoyenera kuchitika mu Church Council.

### 3.1.2 Ntchito za Wachiwiri kwa Wapampando

i. Kuthandiza wapampando mu ntchito zake zonse.

### 3.1.3 Ntchito za Mlembi

i. Kulengeza misonkhano ndi kutumiza mfundo zokambirana kwa nthumwi.
ii. Kulandira mitu ya nkhani zoyenera kulowa pa mfundo zokambirana.
iii. Kulemba mwatsatanetsatane zokambirana mu msonkhano (maminitsi) ndi kuzitumiza pasanathe milungu iwiri.
iv. Kuwerenga zokambidwa mu msonkhano wapita, kukonza apa ndi apo ngati nkofunika.
v. Kusunga maina a nthumwi m'mene aliri pa nthawiyo.
vi. Kutumiza zokambidwa za misonkhano ya Church Council kwa Mlembi wa Parish Council.

#### 3.1.4 Ntchito za Wachiwiri kwa Mlembi

i. Kuthandiza mlembi pa ntchito zake zonse

#### 3.1.5 Ntchito za Msungichuma

i. Kulemba mwa dongosolo ndondomeko ya chuma.
ii. Kulipira zinthu zokhazo zomwe zavomerezedwa ndi Church Council.
iii. Kupereka lipoti ku church council la m'mene ndalama ziliri mwezi uliwonse, ndi kukhala wokonzeka kuwonetsa mabuku kwa akuluakulu monga Bambo Mfumu ndi Msungichuma wa Parish Council.
iv. Kutumiza lipoti la ndalama kwa Msungichuma wa Parish Council.
v. Kuonetsetsa kuti masika ndi ndalama zoyenera kupita ku Parish monga za mtulo, chitukuko, chibalalitso, ndi zithandizo zina zonse zopemphedwa zikufika ku Parish pa nthawi yake.

#### 3.1.4 Ntchito za M'gulupa

i. Ndi mkhalapakati wa Church Council ndi Parish Team.
ii. Ali ndi udindo wolangiza pa ntchito zachikhristu ndi zachitukuko.
iii. Awone mitu yokambirana msonkhano usanachitike ndipo aivomereze.
iv. Angathe kuvomereza chigamulo cha Church Council kapena kuchiimitsa ngati nkofunika kutero mpaka atakambirana ndi Bambo Mfumu.
v. Asule atsogoleri a Church Council.

### 3.2 CHURCH COUNCIL

#### 3.2.1 Zolinga za Church Council

i. Kuzindikira zimene Akhristu akuzisowa kuti athe kutsata chikhristu chawo.
ii. Kulimbikitsa anthu pantchito za chikhristu ndi umoyo.
iii. Kulunzanitsa ntchito za utumiki za Akhristu onse m'deralo
iv. Kulunzanitsa miphakati ndi Parish.

v. Kuzindikira kuti utumiki wawo sukhalira iwo okha koma maganizo a anthu onse okhala m'deralo.
vi. Kulandira ndikugawa thandizo kwa osowa.

### 3.2.2 Udindo wa Church Council

i. Kuchita misonkhano yolunzanitsa ndi yoona kuti ntchito za chikhristu zikuyenda potsata malamulo a Mpingo, malinga ndi dongosolo la Parish ndi Arkidayosizi.
ii. Kulimbikitsa mibindikiro, maphunziro a Akhristu, akatekumeni, achinyamata ndi ena, mabungwe ndi magulu osiyanasiyana kuti moyo wa chikhristu uzame ndi kulimba kuti potero Akhristu akhale mchere ndi nyale pakati pa anthu onse.
iii. Kukonzekera miyambo ikuluikulu ya chipembedzo yomwe ingachitike m'deralo.
iv. Kulimbikitsa ndi kumanga mfundo zolimbikitsira moyo wakudzidalira pa chuma ndi chitukuko, potengera mfundo zikuluzikulu zomangidwa mu msonkhano wa Parish Council
v. Kutenga mfundo, maganizo ndi mavuto a Akhristu a m 'deralo ndikukatula ku Parish Council.
vi. Kupereka maganizo kwa Ansembe pa za chipembedzo.

### 3.2.3 Nthumwi za Church Council

i. Wongolowa chifukwa cha udindo wake-(Mgulupa wotumikira m'derali).
ii. Osankhidwa.
    - Church executive
    - Akulu amiphakati
    - Akulu a mabungwe pa church chonse kuimila mabungwe onse ovomelezeka pa church. Osankhidwa onse ayenera kuvomelezedwa ndi Bambo Mfumu.

#### 3.2.4 Zofunikira kuti wina akhale Nthumwi ya Church /Parish Council

i. Ayenera kukhala Mkhristu wolandira masakramenti, wodzipereka ndiponso wokhulupirika.
ii. Ayenera kukhala wachitsanzo chabwino.
iii. Ayenera kukhala wopereka mokhulupirika mtulo, masika ndi Zina zomwe Mpingo ungapemphe.
iv. Ayenera kukhala wodzipereka ndi wachidwi ku ntchito za Mpingo ndi za chitukuko.

#### 3.2.5 Kuchotsedwa pa Udindo

i. Amene walephera kukwaniritsa zofunika kukhala nthumwi monga mutu 2.6 ukufotokozera, kapena ngati walephera kugwira ntchito yake, adzachotsedwa pa udindo Wake.
ii. Izi zidzachitika pokhapokha Agulupa atafufuza bwino za nkhaniyo ndi kuitula kwa Bambo Mfumu. Pambuyo pake, Bambo Mfumu adzaziwitsa Parish Executive za kuchotsedwa kwa nthumwiyo.
iii. Aliyense amene Parish Council ya tsimikiza kuti wa jomba ku misonkhano itatu yotsatana popanda chifukwa chokwanira adzalankhulidwa, koma akapanda kusintha adzachotsedwa pa mpando. Amene walembera Bambo Mfumu maganizo ake ofuna kutula pansi udindo adzavomeredwa kutula pansi udindowo ngati Bambo adzawona kuti ndikoyenera kutero.

## 4 KUMANGA MPINGO ODZIDALIRA

Kuti tikwanitse ntchito za mpingo, mpingo ukuyenera kukhala ndi chuma chokwanira kuyendetsera ntchitozo. Ma Sinodi awiri oyamba a Arkidayosizi ya Lilongwe a "Mpingo ndife Tonse" ndi "Tiyende Limodzi" analimbikitsa za kumanga mpingo wodzidalira. Zina mwa njira zopezera chuma zomwe zinalembedwa ndi monga;

i. Zopereka za mbale
ii. Ma paper Sunday

iii. Mtulo
iv. Masika
v. Ma business a mpingo

Popeza kuti utsogoleri wa Parish yathu ukuyang'anira ma church angapo, nkofunikanso kukhala ndi ndondomeko yabwino yothandiza kuti ma Church executive a m'parish yathu azigwira ntchito zina za chipembezo ndi chitukuko paiwo okha mounikiridwa ndi a bambo mfumu ndi parish Council. Izi zidzathandiza kuti mpingo uzipita patsogolo, uzichita changu pochita zinthu komanso kupewa kusamvana pakati pa church council ndi parish executive. Mwachidule, pamene outstation yapatsidwa mphavu, zidzathandiza kuti;

- Parish Council izilimbana ndi ntchito zikulu zikulu zokha pa church.
- Akhristu aziwona momwe chopereka chawo chimayendera popeza thumba la Parish limagwira ntchito mma outstation onse.
- A khristu adzakhulupilira kwambiri kuti chuma chomwe amapereka ku mpingo chikugwira ntchito yoyenera.
- Mbale zapadera, monga mbale yachitukuko, izigwira ntchito yokhuzana ndi cholinga chake. Mwachitsanzo, ngakhale tili ndi mbale ya padera ya chitukuko, ndalama zake zimagwira ntchito yoyendetsera church osati Chitukuko. Izi zimakhumudwisa akhristu ndipo ambiri amasankha kusapereka mu mbaleyi kamba kosakhutira ndi ntchito yake.

## 4.1 KUPEZA CHUMA CHOYENDETSERA CHURCH

Popeza kuti chuma chambiri chomwe a khrsitu amapereka ku mpingo monga Mtulo, zopereka za pa misa, ndi masika chimapita m'thumba la parish, nkofunika kuti pakhale ndondomeko yokhazikika yothandizira ntchito za tsiku ndi tsiku pa Church. Ndikofunika kutero chifukwa a khristu omwe amapereka chumachi, amayembekeza kuti zopereka zawo zigwira ntchito yoyendetsa mpingo, kuphatikiza ntchito za pa outstation yawo monga chipembedzo, ukhondo, ndi miyambo yonse yapachaka. Pachifukwa ichi ndikoyenera kuti ndalama zomwe Parish imagwiritsa ntchito pa Church monga kuyendetsa chipembezo ndi kusamala pa church ikhale yokhazikika

ndipo achurch council apatsidwe kuthekera koyendetsa ntchito za tsiku ndi tsiku pa church.

Ndondomeko izi zidzatsatidwa poyendetsa ntchito za tsiku ndi tsiku za Kaggwa Church;

i. Poyamba chaka chilichonse, Kaggwa church executive idzapereka budget yoyendetsera ntchito zawa kwa chaka chonse ku Parish council. Pamene budget yavomeredwa, parish council idzawonetsetsa kupereka ndalama zoyendetsera church kudzera mu bank pa miyezi itatu iliyonse.
ii. Church idzawonetsesa kuti miyambo ya chipembezo ikupatsidwa chidwi chokwanira popanga budget ndi poyigwiritsa ntchito. Church executive idzawonesesa kuti zonse zofunikira pa chipembezo monga ma Baibulo, hostia, mass wine, chimkuza mawu, mipando yokhala zilipo zokwanira.
iii. Church executive idzawonetsetsa kuti zipangizo za umoyo monga zimbuzi zikusamalidwa moyenera ndipo idzapereka zipangizo zoyenera monga zida zokonzera mu tchalitchi nthawi yonse pamene kuli mapemphero ndi alendo.
iv. Ndi udindo wa Church kulimbikitsa a khristu kuti zopereka za pa Church zizipita patsogolo ndi cholinga chokwaniritsa ntchito za outstation.
v. Potsatila dongosolo ili, parish council idzatenga udindo owonetsetsa kuti A treasurer a Church ndi miphakati akupatsidwa upangiri ndi ndondomeko zoyenera kutsatira posamala chuma cha mpingo.

## 4.2 KUGWIRA NTCHITO ZA CHITUKUKO LIMODZI PAKATI PA CHURCH COUNCIL NDI PARISH COUNCIL PA KAGGWA PARISH

Pofuna kulimbikitsa umwini wa ntchito zachitukuko pa church, nkoyenera kuti a khrsitu eni ake azitenga nawo gawo pa ntchito zochitika pa outstation. Kutenga gawo kumayamba pamene akhrsitu apatsidwa mpata wopereka maganizo awo pa kufunika ndi kayendetsedwe ka ntchitoyi. Ndipo pamene parish ikuthandiza ndi chuma pogwira ntchito yachitukuko, ndikoyenera kuti akhristu azitenga gawo losonkha zina mwa ndalama yogwilira ntchitoyo.

Njira izi ndi zina mwa zomwe zidzathandizira kayendetsedwe ka ntchito za chitukuko pa Parish.

i. Zitukuko zonse zopindulira parish yonse monga kumanga ma Church atsopano, nyumba za ansembe, ndi ma business a parish zidzakhala udindo wa Parish Council.
ii. Ma outstation adzapempha zitukuko kuchokera ku parish kudzera mu ndondomeko ya za chuma ndi misonkhano ya parish council.
iii. Parish executive idzasiyira ntchito zachitukuko zokhuza kusamalira church monga kukonza zowonongeka, ukhondo, ndi kusamalira zipangizo za pa outstation mmanja mwa church council ya Kaggwa, kupatula ntchito zomwe zikudutsa mlingo wina wake wa ndalama (ceiling).
iv. Mulingo umenewu udzakhazikitsidwa ndi parish executive potengera upangiri ndi kagwiridwe ntchito ka church executive.
v. Parish idzatha kupereka ntchito yoyendetsa chitukuko ku Church council yoposela mulingo wake (ceiling) malinga ndi chifuniro cha parish executive komiti mogwirizana ndi kuthekera kwa utsogoleri wa Church.
vi. Pofuna kulimbikitsa umwini wa chitukuko, akhrsitu eni ake a pa outstation, adzadziwitsidwa ndi kupatsidwa mpata opereka maganizo awo pa chitukuko kudzera ku miphakati ndi church council.

## 4.3 KUYENDETSA NTCHITO ZACHIFUNDO

Chimodzi mwa zolinga za Church Council (3.2.1) ndi kulandira ndi kugawa thandizo kwa osowa. Pofuna kukwanilitsa zolinga zimenezi, Kaggwa Parish idzatsatila mfundo izi ;

i. Miphakati idzapereka mayina a anthu/mabanja ovutika amene akusowa thandizo losiyana siyana pa moyo wawo wa thupi monga zovala, zokudya, ma school fees ndi zina zambiri.
ii. Maina onse ochokera ku mphakati adzakhala ndi zinthu zomwe anthuwo akusowa.

iii. Mainawa adzaperekedwa kudzera ku office ya Agulupa omwe adzawapereka ku Parish Council.
iv. Parish council idzakhala ndi nthumwi zoyendetsa ntchito yogawa zachifundo.
v. A khristu akufuna kwabwino, omwe ali ndi chidwi chofuna kuthandiza osowa, adzakumana ndi Agulupa kumene adzapatsidwe mwayi osankha vuto lomwe angathe kuthandiza.
vi. Agulupa adzalembera ndi kupereka thandizo lonse lobwera ku parish council.
vii. Parish council, kudzera mu nthumwi zoyendetsa ntchito zachifundo, idzagawa thandizo molingana ndi kaundula wa anthu osowa, yemwe Agulupa alandira kuchokera ku miphakati.
viii. Nthumwi zoyendetsa ntchito zachifundo, zidzawonetsetsa kuti thandizo la anthu osowa likufikira ma church onse a m'parish yathu.
ix. Parish executive ndi Church executive adzathandizana kulimbikisa akhristu kugwira ntchito zachifundo.